


SUE RADER



*Mzimu
Wayera*



Sabata 13: MZIMU WOYERA NDI KULAMBIRA KWA
CIKRISTU.

SUE RADER

Lamulungu:	Aefeso 3:14-19
Lolembe:	Yobu 42:5-6
Laciwiri:	Aefeso 1:15-19
Lacitatu:	Yesaya 6:1-5
Lacinai:	Yesaya 6:6-8
Lacisanu:	Afilipi 3:3
Loweruka:	Masalmo 150:1-2

*Mzimu
Woyera*

Sabata 9: MZIMU WOYERA, NKHOSWE.

Lamulungu: Aroma 10:6-8
Lolembe: Aroma 8:1-2
Laciwiri: Aroma 8:27
Lacitatu: Yohane 1:33
Lacinai: Macitidwe 17:26-28
Lacisanu: Aroma 8:14
Loweruka: 1 Akorinto 2:9-10

Sabata 10: MZIMU WOYERA, MZIMU WACIKONDI.

Lamulungu: 1 Akorinto 13:1
Lolembe: 1 Akorinto 13:2
Laciwiri: 1 Akorinto 13:3
Lacitatu: 1 Akorinto 13:4
Lacinai: 1 Akorinto 13:5
Lacisanu: 1 Akorinto 13:6
Loweruka: 1 Akorinto 13:7

Sabata 11: MZIMU WOYERA, MZIMU WACIWERU-ZIRO.

Lamulungu: Ahebri 10:26-27
Lolembe: Ahebri 10:28-29
Laciwiri: Ahebri 10:30-31
Lacitatu: Yesaya 63:8-10
Lacinai: Yesaya 65:1-2
Lacisanu: Yesaya 1:18-20
Loweruka: Agalatiya 6:1-2

Sabata 12: MZIMU WA CIDZIWITSO NDI KUOPA-AMBUYE.

Lamulungu: Miyambo 2:1-5
Lolembe: Miyambo 1:7
Laciwiri: Miyambo 31:30-31
Lacitatu: Yobu 36:3-4
Lacinai: 1 Atesalonika 4:7-8
Lacisanu: Ezekieli 36:26-27
Loweruka: Masalmo 139:1-6

Sabata 5: MZIMU WOYERA MU MPINGO.

Lamulungu: Yohane 14:26
 Lolemba: Yohane 17:17-19
 Laciwiri: Macitidwe 1:4-5
 Lacitatu: Mateyu 28:19-20
 Lacinai: Marko 16:20
 Lacisanu: Macitidwe 13:2-4
 Loweruka: Macitidwe 10:44-45

Sabata 6: MZIMU WOYERA NDI ANCITO ACE.

Lamulungu: Macitidwe 16:9-10
 Lolemba: Aefeso 6:13-17
 Laciwiri: Yeremiya 1:4-5
 Lacitatu: Macitidwe 4:7-10
 Lacinai: Macitidwe 4:29-31
 Lacisanu: 1 Timoteo 4:1
 Loweruka: Macitidwe 6:3

Sabata 7: MZIMU WOYERA NDI MUNTHU WOCIMWA.

Lamulungu: Yohane 7:37-39
 Lolemba: Yohane 6:33-34
 Laciwiri: Masalmo 95:6-7
 Lacitatu: Masalmo 95:8-11
 Lacinai: Aefeso 4:30
 Lacisanu: Yohane 16:7-11
 Loweruka: Yohane 6:63

Sabata 8: MZIMU WOYERA MPHUNZITSI.

Lamulungu: Yohane 14:15-17
 Lolemba: Yohane 15:26
 Laciwiri: 1 Yohane 5:6-8
 Lacitatu: 1 Atesalonika 4:9-12
 Lacinai: 1 Yohane 2:26-27
 Lacisanu: Yesaya 54:13-14
 Loweruka: Yohane 6:44-46

TABLE OF CONTENTS

PHUNZIRO	TSAMBA
1 KODI MZIMU WOYERA NDANI?.....	1
2 MZIMU WOYERA M'MOYO WA KRISTU.....	5
3 MZIMU WOYERA M'MIYOYO YA ANTHU.....	9
4 MZIMU WOYERA M'KACISI WACE.....	13
5 MZIMU WOYERA MU MPINGO.....	17
6 MZIMU WOYERA NDI ANCITO ACE....	21
7 MZIMU WOYERA NDI MUNTHU WOCIMWA.....	25
8 MZIMU WOYERA, MPHUNZITSI.....	30
9 MZIMU WOYERA, NKHOSWE.....	34
10 MZIMU WOYERA, MZIMU WA CIKONDI.	37
11 MZIMU WOYERA, MZIMU WA CIWERUZIRO.....	41
12 MZIMU WOYERA, MZIMU WA CIDZI- WITSO NDI KUOPA AMBUYE.....	45
13 MZIMU WOYERA, NDI KULAMBIRA KWA CIKRISTU.....	49
ZOWERENGA ZA TSIKU NDI TSIKU ZA M'BUKU LOPATULIKA.....	53

ZOWERENGA ZA TSIKU NDI TSIKU
ZA M'BUKU LOPATULIKA

Sabata 1: KODI MZIMU WOYERA NDANI?

Lamulungu: Ahebri 9:13-14
Lolembe: Yesaya 4:3-4
Laciwiri: Yesaya 11:1-2
Lacitatu: 2 Petro 1:20-21
Lacinai: Masalmo 139:7-10
Lacisanu: Masalmo 139:17-18
Loweruka: 1 Akorinto 2:16

Sabata 2: MZIMU WOYERA M'MOYO WA KRISTU.

Lamulungu: Mateyu 1:20
Lolembe: Yesaya 42:1
Laciwiri: Luka 4:1-2
Lacitatu: Mateyu 12:18-21
Lacinai: 1 Petro 3:18
Lacisanu: Yohane 20:21-22
Loweruka: Marko 1:9-11

Sabata 3: MZIMU WOYERA M'MIYOYO YA ANTHU.

Lamulungu: Oweruza 6:34-35
Lolembe: Oweruza 14:5-6
Laciwiri: Luka 1:13-15
Lacitatu: Luka 1:67-68
Lacinai: Luka 2:25-26
Lacisanu: 2 Mbiri 24:20
Loweruka: Danieli 5:11-12

Sabata 4: MZIMU WOYERA M'KACISI WACE.

Lamulungu: Yohane 2:19-21
Lolembe: 2 Akorinto 6:16
Laciwiri: Eksodo 29:45-46
Lacitatu: Lecitiko 26:11-13
Lacinai: Ezekieli 37:27
Lacisanu: 1 Yohane 4:13
Loweruka: Aroma 8:11

MTSOGOLERI:

Kulambira kwa Cikristu kudzikhala mwa uzimu. Kulambira cabe kwa thupi sikuli kokwanira. Buku Lopatulika limanena kuti tiyenera kumalambira Mulungu mu mzimu ndi m'coonadi. Mulungu afuna kulambira kwathu monga mu zocitika monga izi, kuimba, kupatsa, ndi kumvetsera mau ace, koma zimenezi siziri zokwanira konse ai. Mulungu afuna kuti ifeyo tidzikhala na kulambira kwa mkatikati mwathu. Afuna kuti Mzimu wace atidzadze mitima yathu kotheratu. Ndipozo kuimba kwathu, ndi kupatsa kwathu ndi kumvetsera kwathu ku mau ace kudzakhala ndi tanthauzao lace. Izi zidzakhala zocitika zakulambira kooni ndi koyenera. Pamene ana a Mulungu ali kumulambira iye ndi mayamiko ndi kulemekeza ndi kulola kukera pansi pa mtima mkati. Mulungu adzamva. Tiye ni tipemphere kuti Mzimu wa Mulungu adzatitsogolera kuti tikacite malambiro amtundu, umeneu.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 1

KODI MZIMU WOYERA NDANI?

VESI LOLOWEZA: *"Koma sitinalandira ife mzimu wa dziko lapansi, koma Mzimu wa kwa Mulungu, kuti tikadziwe zimene zipatsidwa kwa ife ndi Mulungu kwa ufulu."*

1 Akorinto 2:12.

LEMBA LOWERENGA: 1 Akorinto 2:10-14.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Buku Lopatulika limanena nthawi zam-biri za Mzimu Woyera kapena Mzimu wa Mulungu. Ngati tiri Akristu tinamva Mzimu Woyera ali kutitsutsa ife za macimo athu ndi kutitsogolera kulandira Kristu. Penanso tinamva kuti ali kutitsogolera kuti tika-cezere bwenzi lathu lomwe silinapululumut-sidwe kapena bwenzi wina yemwe ali kudwala. Koma kodi Mzimu Woyerayu ndi yani? Iye ali kuti? Kodi angatithandizedi kudziwa zomwe tingacite?

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera ali ndi maina ambiri.

Mzimu Woyera ndi Mzimu wa Mulungu yemwe Kristu anatumiza ku dziko lapansi kudzathandiza otsatira ace. Yesu anamucha Iye kuti ndi Nkhoswe kapena Wosangalatsa. "Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale

omi ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona Iye, kapena kumzindikira Iye; cifukwa akhala ndi inu nadzakhala mwa inu." (Yohane 14:16-17). Ndipo adzicha Iye yekha kuti ndi Wotonthoza (Wosangalatsa) mu Yesaya 51:12. "Ine, Onedo, ndine amene nditonthoza mtima wako; kodi iwe ndani, kuti uipa munthu amene adzafa, ndi mwana wa munthu amene adzakhala ngati udzu."

Alinso ndi maina ena ambiri m'Buku Lopatulika. Mwa citsanzo mu mavesi omwe tawetenga mu Yohane, acedwa "Mzimu wa coonadi." Yohanenso auca "kuunika koonadi." Mu Ahebri 9:14 "Mzimu wosatha" anena Mzimu Temweyonse. Aroma 1:4 amuca "Mzimu waciyero." Alinso "Mzimu waciweruziro" ndi "Mzimu wa cinenero" m'buku la Cibvumbulutso. Ndimwe imodzi mu Yesaya, mutu 11; ali nao maina owerengeka a Mzimu Woyera: "Mzimu wa nzeru ndi kuzindikira, mzimu wa uphungu ndi mphamvu, mzimu wakudziwa ndi wa kuopa Ambuye."

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera analipo Paciyambi.

Tingaganizira kuti Mzimu Woyera kunalibe kale asanatimizidwe ndi Yesu kwa otasatira ace. Koma izi sizoonai. Mzimu Woyera anali ndi Mulungu, Atate, ndi Mulungu Mwana, kuyambira pa ciyambi ca nthawi. Iye analipo paciyanbiyambi ndi Mulungu pa cilengedwe. Mu Genesis 1:2 tiwerenga kuti "Dziko lapansi ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa nyanja; ndipo Mzimu wa Mulungu unalinkufungatira pamwamba pa madzi." Popanda Mzimu Woyera

amadziwa kuti Mulungu sadzamvera malekezo ace. Koma Mzimu wa Mulungu uli mkati mwace. Monga tinali kuwerenga mu lemba lathu laphunziro, mzimu amene ali mkati mwathu amatipangitsa kufunafuna Mulungu. Pamene macimo athu atilekanitsa ndi Mulungu, Mzimu amalira mkati mwathu kufikira titampezanso. Atate wathu wakumwamba.

Kamwana kakang'ono komwe kamataya atate wace mcikhamu ca anthu sangathe kuleka kulira. Iye adzalira kolimba kufikira atate wace amumve ndikudza ndi kudzamyamula m'manja mwace. Mkristunso ali tero. Mzimu Woyera mkati mwace amampangitsa kukhala wosakondwa wopanda Mulungu. Amadziwa kuti mpaka atafunafuna kufikira atapeza Atate wace. Ndipo pomwepo adzayesa kucotsa cinthu cimene ciri pakati pa iye ndi Mulungu. Iye adzabvomereza macimo ace kwa Mulungu ndi kupempha Mulungu kuti amkhululukire. Ngati akalibe wosakondwa, adzafunafuna kuti apeze cifukwa cace. Mzimu Woyera yemwe ali mwa iye adzapitirirabe kuitana Mulungu. Ndipo pamene wabvomereza macimo ace onse ndi kutsegula mtima wace kotheratu kwa Mulungu, Mulungu amayankhana. Mzimu amene ali mkati mwace amapatsa cimwemwe ndi mtendere. Ndipo mzimu wace umalemekeza Mulungu. Iye amafuna kukhala ndi Mulungu nthawi zonse. Ndipo coteroye ali wolola kucita kali konse kamene Mzimu wa Mulungu amtsogolera kuti acite. Iye amapereka moyo wace wonse kwa Mulungu. Amapemphera kwa Mulungu kuti agwiritse nchito moyo wace. Amalambira Mulungu podzipereka iye mwini.

GAWO LACIWIRI: Kulambira ndi kulemekeza.

Mulungu amathandiza ao amene apempha thandizo lace. Buku Lopatulika linena kuti, "Potero, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu Wakumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha Iye?" (Luka 11:13). Pena sitingadziwe momwe tingapemphere Mzimu Woyera. Koma ngati tipempha cithandizo ca Mulungu, amatipatsa ife Mzimu Woyera. Mulungu amatithandiza ife kupyolera mwa Mzimu Woyera. Popanda thandizo lace sitingathe ndi pang'ono pomwe kumvera malamulo ace a Mulungu. Koma Mulungu akuti, "Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwako, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwacita." (Ezekieli 36:27). Pamene tiri kuyesa kumacita zinthu zimene tidziwa kuti Mulungu anatifunsa kuti tidzicite, Mzimu Woyera adzatithandiza ife. Mzimu Woyera adzatithandiza kumvesetsa zambiri ndi zambiri. Adzatisogolera kumvesetsa zoonadi za mzimu. Ndipo coteru, Mkristu amaphunzira za Mulungu. Pamene Mzimu Woyera amaulululira za ukuru wace ndi ubwino wace wa Mulungu, Mkristu amaona kudabwitso kwace komwe Mulungu aliri. Amaona kuti iye sali wa mtengo kuti angalandire cikondi ca Mulungu. Komabe, iye ali kudziwa kuti Mulungu amkonda iye. Mtima wace umasefukira ndi mayamiko. Mu pemphero lace, amalonjeza Mulungu kucokera pansi pa mtima wace. Amalambira, Mulungu ndi kulemekeza.

GAWO LACITATU: Kulambiri ndi kudzipereka wekha.

Nthawi zina pamene Mkristu wakhala ali wosamvera, sangalemekeze Mulungu. Iye

anthu amene analemba Cipangano Cakale sakadatha kulemba. Pakuti iye ndiye amene anawauzira iwo kuti alembe, "Pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro ca munthu; koma anthu a Mulungu ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula." (2 Petro 1:21). Yesu atauka kwa akufa ndi kukwera ku kunka Kumwamba, Mzimu Woyera anali kuthandiza ophunzira oyamba a Yesu kuti atsati-re ciphunzitsa ca Yesu ndi kubukitsa mbiri ya bwino ya Kristu. Ndipo Yesu analonjeza kuti Mzimu Woyera adzakhalitsa ndi otsati-ra ace ku nthawi zonse.

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera aliponseponse.

Tawerenga mu Genesis kuti paciyanbi pa cilengedwe mzimu anali kuyenda yenda pamwamba pa madzi. Ngakhale leroli Mzimu Woyera ali mu dziko, kusunga cilengedwe cace kukhala mwa cilongosoko. Mzimu Woyera ali kulankhula kwa osakhulupirira kuyesu kuwadziwitsa ucimo wawo koteru kuti alandire Kristu monga Mpulumutsi wao. Mzimu Woyera ali mkati mwa mitima ya Akristu. Ali kuwatsutsa, kuwatsogoza, kuwapatsa ciyembekezo ndi cimwemwe ndi mtendere.

Cifukwa ali mzimu, Mzimu Woyera sakhalala pa malo amodzi pa nthawi imodzi. Iye sali wa thupi lanyama. Ndipo coteru akhoza kukhala ku malo ali onse pa nthawi imodzimodzi. Kulibe komwe tingapite kuthawa ku Mzimu wa Mulungu. "Ndidzapita kuti kuzambera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzambera nkhope yanu?" Masalmo 139:7. Buku Lopatulika lititsimikizira kuti kulibe malo komwe munthu angazembere Mzimu Iye aliponseponse.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amadziwa zonse.

Pali nthawi zambiri pamene timasowa nzeru. Koma sitiri a nzeru. Tisowa than-dizo. Mzimu Woyera ali wokoza kutithan-diza. Iye ali wanzeru koposa ife. Palibe nzeru zina ziri zonse zomwe mungayerekeze nazo nzeru za Mulungu. Iye ali wa nzeru koposa munthu aliyense yemwe anakhalako mu dziko lapansi ndi kale lonse. "Ha! kuya kwace kwa kulemera ndi kwa nzeru ndi kwa kudziwa kwace kwa Mulungu! Osasanthulik-adi maweruzo ace ndi njira zace nzosalon-doleka! Pakuti anadziwitsa ndani mtima wace wa Ambuye. Kapena anakhala mphungu wace ndani?" (Aroma 11:33-34).

"Ndani anapangira mzimu wa Yehova, kapena kukhala phungu lace ndi kuphunzitsa Iye." (Yesaya 40:13). Palibe wina aliye-nse amene angayese kuyesa Mulungu. Njira yace iri nthawi zonse njira yoposa. Koma nthawi zina tikadziwa kuti Mzimu Woyera ali kutitsogolera, timacita kanthu kena. Pamene tiri kucita kanthu kotereka tiri ku-nena m'mitima mwathu, "Mulungu, njira zan-ga ndizo zoposa zanu." Uku ndi kucimwa. Tidzisamalira kutsatira Mzimu Woyera ngati tikhulupiriradi kuti ali wanzeru.

MTSOGOLERI:

Mzimu Woyera adzatitsogolera ife ku moyo wocuruka. Cifukwa ali naco cidziwitso ca Mulungu, ndipo amamva m'njira ya Mulu-ngu. Ndipo angofotokoza njira zimenezi kwa ife ngati tim'lola. Kristu anatomaza Mzimu Woyera "kutitsogolera m'coonadi conse." Ndipo Kristu akuti coonadi cidzakumasulani inu.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

PHUNZIRO 13

MZIMU WOYERA KULAMBIRA KWA
CIKRISTU

VESI LOLOWEZA: *"Mulungu ndiye mzimu; ndi-po molambira Iye ayenera kumlambira mu mzimu ndi mcoonadi."*

Yohane 4:24.

LEMBA LOWERENGA: Agalatiya 4:6.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Mwana amakonda atate wace ndi amace. Iye amakonda kuti adzikhala nao. Iye amafuna kuti iwo adzikondweretsedwa ndi zinthu zomwe iye acita. Ngati wacita kanthu kena amakondweretsa Mulungu. Iye ali Mwana wa Mulungu. Mzimu wa Mwana wa Mulungu uli mkati mwa Mkristu. Mzimu ameneyu amamtsogolera Mkristu mu ciyanjano cace kwa Mulungu Atate.

GAWO LOYAMBA: Kulambira ndi mayamiko.

Mkristu amazindikira kutikopanda Mulungu sakadakhala kanthu. Elihu anati, "Mzimu wa Mulungu unandilenga ine, Ndi Mweya wa Mphamvu yonse unandipatsa moyo." (Yobu 33:4). Mkristu amadziwa kuti moyo wace utsamira pa Mulungu. Ngati Mulungu sanafuna kuti iye akhale ndi moyo, akadakhala wafa kale. Iye amadziwa kuti Mulungu ali ndi colinga ca moyo wa iye mwini Amalambira Mulungu ndi mayamiko a moyo wace. Ndipo amapemphera kwa Mulungu kuti amtsogolere kuti apeze kutanthauza kwace kwa moyo.

abwnezi lathu. Iye anasankha kuonetsera cilengedwe cace kwa ife kupyolera mwa Mzimu wace mwini. Watilola ife kuphunzira njira zace kotero kuti tikhoze kumtsatira. Watipatsa ife Mzimu Woyera mkati mwa mitima yathu kotero kuti akhoza kumakhala nafe nthawi zonse. Pamene tiri kuphunzira za iye, tiyenera kumadziwa kuti amatisamalira ife. Pamene tiri kudziwa zambiri za Iye, timkhulupirire koposa. Tiyeni timfunse kuti alowe mbali iri yonse ya moyo wathu. Tiyeni tipemphere kuti akhale wolamulira zinthu zonse zimene ticita.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 2

MZIMU WOYERA M'MOYO KRISTU

VESI LOLOWEZA: *"Taona Mtumiki wanga, amene ndimgwiriziza; Wosankhika wanga, amene moyo wanga ukondwera naye; ndaika mzimu wanga pa Iye; Iye adzaturutsira amitundu ciweruziro."*

Yesaya 42:1.

LEMBA LOWERENGA: Luka 4:18.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Ngati tilandira Kristu monga Mpulumutsi wathu talandiranso kumakhala monga iye. Tiyeni tiyang'ane moyo wa Yesu ndi kuona momwe Mzimu Woyera anali kumuthandizira iye mu zonse zimene anacita.

GAWO LOYAMBA: Kubadwa kwa Yesu.

"Ndipo kubadwa kwace kwa Yesu Kristu kunali kotere: Amai wace Mariya anapalidwe ubwenzi ndi Yosefe, koma asanakomane iwowo, anapezedwa iye ali ndi pakati mwa Mzimu oyera." (Mateyu 1:18). Yesu sanali mwana wa Yosefe. Mariya anapalidwa ubwensi ndi Yosefe koma anali asanakwatirane. Mzimu Woyera anadza pa Mariya ndipo anakhala ndi pakati. Yosefe anali kuopa zomwe anthu adzanena. Ndipo coteru anali kuyesa kupeza njira ya kuti asakwatirane naye Mariya. Iye sanamfuna Mariya ngati anali ndi mwana wa mwamuna wina. Koma mngelo anadza

kwa iye namuuzwa iye kuti Mariya sanakhala wosakhulupirika kwa iye ai. Mngelo anamuuzwa Yosefe adayenera kukwatirana naye Mariya. Iye anali ndi pakati mwa Mzimu Woyera. Onani Mateyu 1:20.

GAWO LACIWIRI: Zimene zinacitika ndi Yesu.

Werengani Mateyu 3:16-17. Pamene Yesu anali kukula msinkhu Iye anali kutso-gozedwa ndi Mzimu Woyera. Pamene anakula msinkhu, anapita ku Mtsinje wa Yordano komwe Yohane anali kubatiza. Kumeneko anamfunsa Yohane kuti ambatize iye. Ndipo pamene anaturuka kucoka m'madzi Mzimu Woyera anatsika kucoka kumwamba nakhala pa iye. Ndipo mau ocokela kumwamba ananena kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu. Buku Lopotulika linena zambiri zomwe zinacitika m'moyo wa Yesu atabatizidwa. Monga momwe tinawerenga zina za izo, tidziwadi kuti Mzimu Woyera anali kumtsogolera iye.

GAWO LACITATU: Kuyesedwa kwa Yesu.

Mzimu Woyera anamtsogolera Yesu kunka ku cipululu kukayesedwa ndi Satana. Iye sanamtuma kuti akayesedwe ali yekha konse ai. Mzimu anapita naye Yesu kukamthandiza kulimbana ndi Satana. Akhoza kutithandiza ifenso mu njira imodzimodzi. Nthawi zambiri timamvaathu ali kunenakuti, "Sindiri wolimba kuti ndingalimbane nao mayesero." Koma tizizindikira kuti Mzimu Woyera ali wamphamvu kutha kutithandiza ife. Iye ali wamphamvu koposa mayesero ena ali onse. Ndipo akhoza kutithandiza ndi kutipatsa mphamvu yakunena kuti, "Toto, sindingacite tero. Mulungu sangafune kuti ine nditero."

ndi Ambuye. Citanthauza kuti timadziwa nthawi zonse kuti Mulungu alipo Iye tidziwa kuti anatilenga. Titsimikizadi kuti ali kutitsogolera. Timakumbukira kuti Yesu ndiye Mbuye wathu. Sitiwala konse zonze zimene Yesu anaticitira ife. Zonse zimene timacita zimanena kuti, "Zikomo Ambuye, pondipulumutsa ine."

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amatipatsa ciyembekezo.

Yesu anatilonjeza kuti tidzakhala naye mkati mwathu. Mzimu Woyera amatipatsa ciyembekezo kuti izi nsoonadi. Yesu mwini wace ananena kuti, "Koma pamene wafika Nkhoswe, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kucokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa coonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandizitira Ine umboni." (Yohane 15:26). Mzimu Woyera ndi mboni amene Yesu adzasungamolonjezani lace la kwa otsatira ace. Iye tikhulupirira kuti Yesu adzatilipira ife pokhala monga momwe Iye afunira. Mzimu Woyera amene ali mwa ife ndiye citsimikizo cathu. "Kuti ife amene tinakhulupirira Kristu kale tikayamikitse ulemetero wace. Mwa Iyeyo inunso, mutamva mau a coonadi, Uthenga Wabwino wa cipulumutso canu, ndi kumkhulupirira Iye, munasindikizidwa cizindikilo ndi Mzimu Woyera wa lonjezani." (Aefeso 1:12-14).

MTSOGOLERI:

Pamene tiri kupemphera, tiyeni tiyamike Mulungu potipatsa Mzimu wace. Tiyeni timuyamike iye cifukwa ca nzeru zace ndi mpahmva. Tiyeni tikumbukire kuti tiri opanda pace. Sitiyenera kanthu kali konse komwe tilandira kucoka kwa Mulungu. Komabe ngakhale ndi tero anasankha kukhala

Mzimu wace Woyera. Ndipo coteru ndi Mzimu amene amatitsogolera kuti tilandire Yesu monga Mpulumutsi wathu. Iye sitingadze kwa Yesu tokha, wopanda Mzimu woyera. Pali wina aliyense amene angatikakamize kumtsatira Yesu ngati Mzimu Woyera sali kutionetsera ucimo wathu. Ndipo coteru ndi Mzimu Woyera amene amayemba kutionetsera ife kwa Yesu.

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera amatiphunzitsa za Yesu.

Titamdziwa Yesu kuti ndi Mpulumutsi wathu, ndi Mzimu Woyera amene amaulula zambiri za Yesu. Ao amene akhala Yesu asanabedwe sanamvetse momwe adzabwerera. Iwo anali kuyang'anira wolamulira wa dziko lapansi yemwe akadadzawamasula m'manja a adani ao. Koma Yesu anadza kudzamasula munthu kucoka kwa mbuye wa mtundu wina, ucimo. Mzimu Woyera amatithandiza kumvetisa za kuzizwitsa kwake kwa Kristu. Mu Aefeso 3:4-5 Paulo anena kuti, "Cimene mukhoza kuzindikira naco pakuciwerenga, cidziwitso canga m'cinsinsi ca Kristu, cimene sanacizindikiritse ana a anthu m'mipadwo yina, monga anacibvumulutsa tsopano kwa atumwi ndi aneneri ace oyera mwa Mzimu." Pali zinthu zambiri zonena za Kristu zimene sitingathe kudzifotokoza. Koma Mzimu Woyera amatithandiza kudziwa kuti zinthuzi ziri zoon. Iye amatipatsa cikhulupiriro.

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera amatipatsa kuopa Ambuye.

Pamene Mzimu Woyera ali mkati mwathu, amatipatsa ife kulimba mtima ndi mphamvu zomwe tisowa kuti tikhale monga Akristu. Amatithandiza "kuyenda mukuopa Ambuye." Ici sicitanthauza kuti tiri kucita mantha

GAWO LACINAI: Zozizwitsa za Yesu.

Yesu Kristu anacita zizizwitsa zambiri. Iye anathandiza anthu omwe anali odwala kwambiri. Anathandiza anthu omwe anali osaona kuti aone. Anapatsa mphamvu kwa ao amene anali opunduka koteru kuti anayenda. Anathandiza ao amene anali ndi mizimu yoipa kuti anatha kudziganzira okhanso. Afarisi anali kuganiza kuti Yesu anali ndi mphamvu yocokera kwa Satana. Koma Yesu anawafotokoza kuti Satana sangapatse mphamvu zakuti aononge nchito zake zomwe. Ndipo Iye amene aononga nchito za Satana ayenera kukhala wa mphamvu koposa Satana mwini. Yesu ananena nati, "Koma ngati Ine ndimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yake ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu." (Mateyu 12:28).

GAWO LACISANU: Imfa ndi Kuunkanso kwa Yesu.

Cifukwa ca Mzimu Woyera, Yesu anatha kufa pamtanda ndi kuunkanso kwa akufa pa tsiku la citatu. Onani Petro Woyamba 3:18. Mzimu Woyera anapatsa Yesu mphamvu ya kukhala moyo wopanda ucimo koteru anatha kudzipereka yekha nsembe ya macimo athu onse. Pomweponso Mzimu anapatsa Yesu mphamvu yakugonjetsa imfa kuti iye ataitsimikizire za moyo wosatha.

MTSOGOLERI:

Yesu anadzazidwa ndi Mzimu Woyera moyo wake wonse. Iye anazindikira mphamvu ya Mzimu Woyera m'moyo wake ndipo anafuna kuti otsatira ace akhale nayo mphamvu yomweyonse. Iye anati, "Mtendere ukhale ndi inu. Monga Atate anandituma Ine, ndikutu mani Inenso." Iye sanawatumiza iwo okha.

Atate wace sanamtumiza iye yekha. Atangon-
ena mau amenewa anawapatsa Mzimu Woyera.
Werengani Yohane 20:21-22. Yesu afuna kuti
otsatira ace adzikhala monga iye koma ad-
ziwa kuti palibe munthu yemwe angathe ku-
tero mwa iye yekha. Ici ndico cifukwa
cace anatipatsira ife Mzimu Woyera. Tidzi-
lola Mzimu Woyera kuti atithandize ngati
tifuna kuti timtsatire Yesu.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 12

MZIMU WOYERA, MZIMU WACIDZIWITSO
NDI WAKUOPA AMBUYE

VESI LOLOWEZA: *"Kuti Mulungu wa Ambuye
wathu Yesu Kristu, Atate
wa ulemmerero, akupatseni
inu mzimu wa nzeru, ndi
wabvumbulutso kuti mukam-
zindikire Iye."*
Aefeso 1:17.

LEMBA LOWERENGA: Yesaya 11:2.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Cikristu ncopusa kwa ao amene samd-
ziwa Yesu. Iwo sanalandirepo Mzimu Woye-
ra m'mitima mwao. Ndipo coteri sanawathan-
dizapo kuti amvesetse zoonadi za mzimu.
Pena anawapangitsa kuti adziwe kuti ali
ocimwa. Koma mpaka wina atalandira Mzimu
Woyera, samdziwa Mulungu. Mzimu Woyera
amatipatsa ife cidziwitso ca njira ca Mu-
lungu.

GAWO LOYAMBA: Mzimu amatisogolera ku cip-
ulumutso.

Tisanalandire Mzimu Woyera, iye ana-
lankhula mkati mwathu. Iye anatithandiza
kukhulupirira kuti Yesu anafera macimo a
athu. Yesu anati, kulibe mmodzi akhoza
kudza kwa Ine koma ngati Atate, wondituna
Ine amkoka iye; ndipo Ine ndidzamuukitsa
iye tsiku lomariza." (Yohane 6:44). Mu-
lungu Atate amalankhula nafe kupyolera mwa

Tonsefe timacita ucimo. Ndipo coterotiyenera kumapempha cikhululukiro. Tidzikhala osamalira kuti sitilola wina wa ciwalo campingo wathu kumapitirizabe mu ucimo. Ngati tibvomerezana nao ucimo wace pomacita monga ngati sitiudziwa umino wace, tiri kunama pamaso pa Mulungu. Tiyeni aliyense wa mupingo mwathu akhale wokhulupirika ndi woona kwa Mzimu Woyera. Tiyeni aliyense alape macimo ace. Tiyeni tisa-patsa Mzimu Woyera cifukwa cakuti akwiysidwe ndi mpingo wathu.

MTSOGOLERI:

Mzimu Woyera safuna kuti anthu ace adzikhala osamvera. Iye safuna kukhala Mzimu wa Ciweruziro. Buku Lopatulika lina kuti amamva cisoni pamene ana ace acita zonyansa. Tiyeni tipemphere kuti adza-tipatsa mphamvu ndi kulimba mtima kupitiriza kumtsatirabe ndi kulimbana nao mayesero omwe timakomana nao kuti aticimwitse.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 3

MZIMU WOYERA M'MIYOYO YA ANTHU

VESI LOLOWEZA: *"M'menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, cifukwa anatipatsako Mzimu wace."*
1 Yohane 4:13.

LEMBA LOWERENGA: Yobu 32:5-10,18.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Buku Lopatulika litiuza za anthu ambiri mane anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Iye anapatsidwa nzeru ndi Mulungu kutsogolera anthu ace kapena kucita nchito inayace. Ena a anthu amenewa anali anyamata. Nthawi zina anali kutsogolera anthu omwe anali akulu koposa iwo. Nthawi zina anali kumatsogolera mafulu akuru a anthu. Nthawi zina anali kumapanga zisankho zobvuta ndi zolimba. Koma Mulungu anali kuwapatsa Mzimu wace kuwathandiza.

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera anathandiza Yosefe.

Ngati munthu watsogozedwadi ndi Mzimu wa Mulungu, ngakhale osakhulupirira adzaona kuti ali munthu wa nzeru ndipo adzamacitira iye ulemu. Yosefe anakhala mu dziko la Aigupto pakati pa anthu omwe sanakhulupirira mwa Yehova. Koma Farao, wolamulira wa dziko la Aigupto, analota loto. Anthu

onse a nzeru amu Aigupto analephera kumasulira lotolo la Farao. Yosefe anaitinani-dwa ndipo anamasulira kutanthauza kwace kwa loto la Farao. Ndipo pamene Yosefe anamasulira lotoli kwa Farao, ngakhale Farao mwini ananena kuti Yosefe anali wanzeru kwambiri. Ndipo iye anazindikira kuti ndi mzimu wa Mulungu wokha womwe ukhoza kupanga munthu kukhala wa nzeru. "Ndipo Farao anati kwa anyamata ace, Kodi ife tidzaone munthu ngati uyu, mzimu wa Mulungu uli m'mtima mwace?" (Genesis 41:38).

GAWO LACIWIRI: Mzimu wa Mulungu anathandiza Bezaleli.

Mulungu sangoptsa Mzimu wace kwa anthu kuti akhale auphungu kokha ai. Pena Mulungu amafuna kuti munthu acite kanthu ndi manja ace. Mzimu Woyera amamthandiza kuti akhale m'misiri wabwino kotero kuti nchito yace ikondweretse Mulungu. Buku Lopatulika linena za munthu monga ameneyu mu Eksodo 31. Mulungu anafuna kuti Bezaleli akhale woyang'anira mamangidwe akacisi. Iye anafunika kudziwa kamangidwe ka kacisi, likasa la cipangano ndi mpando wacifundo, guwa lansembe, ndi zinthu zonse zamukacisi. Ndipo coter Mulungu amamthandiza kuphunzira kudziwa kupanga zinthu zimenezi. Eksodo 31:3 akuti, "Ndipo ndamdzaa ndi mzimu wa Mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi zidziwitso, ndi nchito ziri zonse."

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera anathandiza Yoswa.

Mulungu anafuna munthu akuti atsogolere anthu ace kulowa mu dziko la lonjezano. Iye anafuna munthu yemwe anali wopanda mantha, munthu yemwe anakhulupirira

m'mawa mwace aja amene anasiyidwa anayamba nso kukaika ulamuliro wa Mose. Ndipo Mulungu anawaononganso nao. Tidzilola Mzimu Woyera kuti adzisankha atsogoleri m'mipingo mwathu. Ngati wina adzipanga yekha kukhala mtsogoleri, pena sanasankhidwa ndi Mulungu. Pena angatisogolere kucoka kwa Mulungu. Ndipo ngati titsatira, Mzimu Woyera angakwiye ndi khamu lonse. Tidzifunafuna citsogozo cace kotero kuti tidzadziwa kuti kodi ndani amene tingamtsatire.

GAWO LACITATU: Ciweruziro ca munthu payekha.

Mulungu samaweruzza khamu lonse la anthu cifukwa cakuti munthu mmodzi acaci-mwa. Mu lemba lathu lapunziro taonamo nthano ya Hananiya ndi Safira. Awiriwa anali mu mpingo. Ndipo mpingo wao unaganizira kuti onse afulitse zonse zimene anali naco ndikudzanazo ndaramazo ku mpingo. Ndipo munthu aliyense anali kufunika kusankha kuti kodi atero kapena ai. Munthu aliyense anali kusankha yekha kuti pena apereke theka kapena zonse. Hananiya ndi Safira anagulitsa munda wao koma iwo anaganizira zakupereka mbali cabe ya ndarama zaozo. Komabe, iwo anafuna kuti akhale omveka mu mpingo. Ndipo iwo anaganiza kumena kuti ndarama zonse zinali zimenezo.

Petro, mtsogoleri wa mpingo, anawafunsa iwo pamaso pa khamu lonse. Mzimu Woyera anaonetsera ucimo wao. Anakwiya kwambiri cifukwa ananama kwa iye. Ndipo onse awiri anafa tsiku lomwe lija. Koma mpingo ubalibe mbali mu ucimo wao. Ziwalo za mpingo sidzinagwirizana ndi zomwe anacita. Ndipo coter Mulungu sanalanga mpingo cifukwa ca ucimo wa awiriwa.

mu dziko la Aigupto ku dziko la ukapolo. Anali nao paulendo wautari kunka ku dziko la lonjezano anawamenyera nkondo ya adani ao. Koma tsopano iwo anampandukira. Anakana kumtsatira Mulungu. Ndipo anapembenda munga akunja anacitira. Cifukwa ca cimeneci Mulungu anakwiya nao kwambiri. Ndipo analola kuti ciweruziro cace cigwe pakati pa Israeli. Analola kuti adani ao awakhonjetse. Analola kuti atengedwe kunka ku dziko la ukapolo.

GAWO LACIWIRI: Ciweruziro ca khamu.

Pena sitibvomereza kuti Israeli akadaweruzidwa cifukwa ca kuipa kwa mtungu wonse. Koma nthawi zina Mulungu amaweruzacigulu conse ca anthu cifukwa ca ucimo wa munthu m'modzi. Muli nthano yotereyi mu Cipangano Cakale. Mulungu anasankha Mose kuti atsogolere anthu ace. Ndipo Mose anali kuwatsogolera munga momwe Mulungu anamtsogozera. Koma munthu wina wocedwa Kora anamneneza Mose kuti anangodzipanga yekha kukhala mtsogoleri. Ndipo Kora anayambitsa madandaulo pakati pa anthu. Mulungu anakwiya kwambiri ndi Kora ndi onse amene anamumvera iye. Mulungu anali kukonza kuti aononge onse amene anali kudanfaula. Ndipo Mose ndi Aroni anapepetsera anthu aja. "Ndipo anagwa nkhope zao pansi, nati, Mulungu, ndinu Mulungu wa mizimu ya anthu onse. walakwa munthu mmodzi, ndipo kodi mwakwiya nalo khamu lonse." (Numeri 16:22). Mulungu anali wokonzeka kuweruza anthu akhamu lonse cifukwa analola kuti munthu mmodzi awatsogolere kucoka kwa iye. Iye anakwiya ndi anthu ambiri cifukwa anatsatira munthu amene sanasankhidwa ndi iye. Ndipo Mulungu anamvera Mose nawasiya onse kusiya ao okha amene anayesetsa kuti akhale atsogoleri pamodzi ndi Kora. Komabe,

citsogoza ca Mulungu. Ndipo coteri anasankha Yoswa. Anamuuza Mose kuti, "Utenge Yoswa mwana wa Nuni, ndiye munthu mwa iye muli mzimu, nuike dzanja lako pa iye." (Numeri 27:18). Yoswa ananeotsera poyamba kuti anakhulupirira mwa Mulungu. Pamene anali m'modzi wa azondi omwe anatumidwa kukazonda ndi kubwera ndi mbiri ya Dziko la Lonjezano, ndi iye yekha ndi Kalebi amene anakumbukira kuti Mulungu ananena kuti adzathandza Israeli kutenga dzikolo. Momwe ana a Israeli anayendera mu cipululu kwa zaka makumi anai cifukwa sanakhulupirira Mulungu. Mulungu anadziwa kuti munthu ngati Yoswa akhoza kucita nchito. Anadziwa kuti munthu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera adzakhalabe wolimba mtima ndi wa mphamvu.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera anathandiza Stefano.

Mpingo woyamba unafuna kusankha amuna omwe adzathandiza pakutumikira Ambuye. M'modzi wa amuna omwe anasankhidwa anali Stefano. Buku Lopatulika likuti anali "mwamuna wodzala ndi cikhulupiro ndi wa Mzimu Woyera." Cifukwa cakuti anali mtsogoleri wa bwino, mau a Mulungu anacuruka, ndi ciwerengero ca ophunzira cinaonjezeka koposa. Stefano anatsatira Mzimu wa Mulungu nthawi zonse koteri kuti adani a Yesu anakhalanso adani acenso. Ndipo optsiriza anamponya iye miala mpaka kufa. Koma pamene anali kufa, anadziwa kuti Mzimu Woyera anali naye ndipo sanacita mantha

MTSOGOLERI:

Anthu a Mulungu nthawi zonse amasowa mtsogoleri yemwe wadzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu. Iye angakhale mnyamata kapena

angakhale wacikulire. Koma ngati ali ndi Mzimu Woyera mkati mwa mtima mwace, adzakhala ndi nzeru zakutsogolera mpingo. Ngati Mulungu afuna munthu kuti atsogolere, adzampatsa mphamvu ndi nzeru ndi kulimba mtima. Mulungunso adzampatsa mwai wa kutsogolera. Mulungu safuna munthu kuti adzipange yekha kukhala mtsogoleri. Nthawi zina Mulungu sali wokonzeka kuti munthu uja atsogolere.

Aliyense wa ife adzilola Mzimu Woyera kuti adzaze m'yoyo yathu kotheratu. Tidzimkhulupirira Iye kutitsogolera tsiku ndi siku. Tidzikhulupira Mulungu kusankha mmodzi kuti atsogolere anthu ace. Ziwalo za mpingo zidzifunsa Mzimu Woyera kuti awatsogolere kusankha atsogoleri oyenera. Mulungu adzawaululira iwo "munthu amene mwa iye muli mzimu."

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 11

MZIMU WOYERA, MZIMU WACIWERUZIRO

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo mutani, kulanga koposa kotani nanga adzayesedwa woyenera iye amene anapondereza Mwana wa Mulungu, nayesa mwazi wa cipangano umene anayeretse-dwa nao cinthu wamba, nacitira cipongwe Mzimu wa cisomo."*

Ahebrei 10:29.

LEMBA LOWERENGA: Macitidwe 5:3-4.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Takhala tiri kuphunzira momwe Mzimu Woyera aliri mthandizi wathu. Koma lero tifuna kuona zifukwa zomwe Mzimu Woyera angakhaliwe wotitsutsa. Ngati timlola iye kuti alamulire myoyo yathu, pamenepo ndi bwenzi lathu labwino koposa. Koma ngati tamupandukira iye, amakhala mzimu wa ciweruziro.

GAWO LOYAMBA: Ciweruziro ca amitundu.

Werengani Yesaya 63:10. Anthu amene ali mu nthano imeneyi anali anthu a mtundu wa Ciyuda. Iwo anali anthu osankhika a Mulungu. Iye analonjeza lonjezano kwa Abrahamu kuti adzawapanga kukhala mtundu wa anthu. Iye anawatsogolera kunka ku dziko la Aigupto ku wacinjiriza ku njala. Iye anawathandiza kuti akhala ndi ana ambiri amuna ndi akazi. Anawathandiza kuturuka

GAWO LACINAI: Tidzikonda adani athu.

Ngati tikonda ao amene ali m'banja lathu ndi kukonda ao amene ali mu mpingo mwathu, ndipozo tikhoza kukonda adani athu. Yesu ananena nati, "Aliyense angakonde bwe-nzi lace, koma inu mudzikondana nao adani anu." Ici ndi cinthu cosatheka kucitika popanda thandizo la Mzimu Woyera. Cifukwa ali mzimu wa cikondi, akhoza kutipatsa ife cikondi ngati akhala m'mitima mwathu. Ti-ngakonde adani athu ndi thandizo la Mulu-ngu. Ngati Mzimu Woyera ali mkati mwathu, tidzatha kukonda ao amene adana nafe, ao amene aticititsa kuti iwo apeze phindu la iwo eni, ao amene ali a nkhave kwa ife.

MTSOGOLERI:

Mulungu afuna kuti tidzimkonda Iye. Koma sitingathe kuonetsa cikondi cathu kwa iye kufikira titasunga malamulo ace akukon-dana wina ndi mnzace. Yesu ananena nati, "Ngati mukonda Ine, sungani malamulo anga." Mzimu Woyera adzatitsogolera ife kukonda anthu onse. Koma tidzikhala olola kutsa-tira citsogozo cace. Ngati timtsatira ndi kuphunzira kuonetsa cikondi cace kwa onse amene tikomana nao, adzadziwa kuti timkon-dadi. Kungonena kuti timkonda iye nkosa-kwanira konse ai. Tiyenera kumaonetsera cikondi cathu.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 4

MZIMU WOYERA M'KACISI

VESI LOLOWEZA: *"Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndikuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu."*

1 Akrointo 3:16.

LEMBA LOWERENGA: 1 Yohane 3:24.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Zipembedzo zambiri ziri ndi makacisi ao komwe otsatira ao amapita kukalambira milungu yao. Ena amakhulupirira kuti mi-lungu yao imakhalitsa mu akacisi amenewa. Koma Cikristu siciri cotere ai. Akristu amamanga nyumba za macalici koma izi ndi zinyumba cabe momwe mipingo imakomaniramo pamodzi. Akristu salambira Mulungu mu nyu-mba za macalici ndipo nthawi zambiri. Mu-lungu amakhala alipo pompo. Koma Mulungu sakhalala nyuma za calici. Mulungu sakhalala mnyumba iri yonse. Komabe, Mulungu ali naye kacisi. Buku Lopatulika likuti Akri-stu iwo eni ali akacisi a Mulungu. Mulu-ngu akuti tiri kacisi wace ngati tapatsa mitima yathu kwa Iye.

GAWO LOYAMBA: Lolani Mzimu Woyera Adze m'kacisi wace.

Coyamba tiyenera kumlola kuti adze mkacisi mwace. Ngati tikhulupira mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wathu, tibvomereza macimo athu kwa Iye. Yesu amatikhulukira ife natipatsa Mzimu wace Woyera. "Koma

Petro anati kwa iwo, lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza kucikhululukiro ca macino anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera." (Macitidwe 2:38). Munthu aliyense ali nao mwai wakutsa ku kacisi wa Mzimu Woyera. Ziribe kanthu kaya ndife ayani, timakhala kacisi wa Mzimu Woyera pamene adza m'miti-ma mwathu.

GAWO LACIWIRI: Sungani kacisi kukhala wanguwiro.

Mzimu Woyera afuna kuti matupi athu akhale kacisi wace. Werengani kaciwili vesi loloweza. Buku Lopatulikanso likuti, "Cifukwa cace ndikupemphani inu abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera." (Aroma 12:1-2). Tidzikhala osamalira kusunga matupi athu kukhala olandirika pamaso pa Mulungu. Ngati ticititsa mathupi athu kucita ucimo, sitiri olandirika. Mzimu wace Woyera safuna kukhala mkacisi yemwe ali wa dothi ndi wodetsedwa. Werengani Akorinto Woyamba 6:15-20. Mulungu safuna kuti tidzicita kanthu kena kali konse komwe sikamcitira ulemmerero Iye. Lemba lathu lowerenga likuti iye akhala mwa iwo amene asunge malamulo ace. Yesu anati lamuli loyamba nilakuti, "Udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse." (Mateyu 22:37). Sitingamkonde Mulungu m'njira yotere ndipo nkumacita zinthu zina zomwe zitsutsana ndi cifuniro cace. Ngati timkonda iye, tifuna kumkondweretsa iye. Yesu ananena nati, "Ndi lina lofanana nalo pali, Udzikonda mnansi wako monga udzikonda iwe mwini." (Mateyu 22:39). Ici sici-thathauza abwenzi athu okha. Mnansi wathu

koma m'modzi. Ndipo zimene Mulungu wacimanga pamodzi, palibe munthu adzazimasula." Mwamuna asamakwiwira kapena kusakondwera naye mkazi wace. Adziyesa kukhala naye mucigwirizano. Asamaganiza zakumuleka. Ana amaonetsa kuti akonda Mulungu pamene amvera makolo omwe Mulungu anawapatsa. Makolo adzisamalira kwambiri pamene ali kudzudzula ana ao. Onetsani cifundo monga Mulungu anaonetsa cifundo. Phunzitsani mwana kuti adzikonda Mulungu ndi kumacita zabwino. Koma mukhale okhululukira monga momwe Mulungu ali wakukhulukira. Tidzifunsa Mzimu Woyera kutithandiza kupanga mbanja athu kukhala malo acikondi.

GAWO LACITATU: Kukonda ao amene ali mu Mpingo.

Werengani 1 Petro 1:22. Pamene tiri kuphunzira kumvera Mzimu Woyera, tiphunziranso kukondana wina ndi mnzace. Tikon-da ena omwe ali mumpingo mwathu. Timayesetsa kumvesetsa za anzathu wina ndi mnzace. Monga tiri okhululukira. Tiri opanda dyera. Tinalamulidwa kuti tikondane wina ndi mnzace momwe Yesu anatikondera ife. Iye anapereka moyo wace cifukwa ca ife.

Pamene tiri kukondana wina ndi mnzace tiri kutsatira Mzimu Woyera tidzakhala nawo umodzi mu mpingo mwathu. Buku Lopatulika linena kuti, "Anthu a m'dziko amacititsa m'patukano," koma ife Akristu tidzipemphera mwa Mzimu Woyera, Mzimu Wa cikondi. Mulungu afuna ao amene apemphera pamodzi adzikondana wina ndi mnzace. Iyindiyo nzeru yace ya mpingo. Mzimu Woyera adzatsogolera mpingo womwe ukondana wina ndi mnzace.

"Koma iye amene akasunga mau ace, mwa iye-yu zedi cikondi ca Mulungu cathedwa. M'menemo tizindikira kuti tiri mwa Iye; iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wace kuyenda monga anayenda Iyeyo." (1 Yohane 2:5-6). Timaonetsera cikondi cathu kwa Mulungu posunga malamulo ace. Koma lamulo loyamba n'lakuti "kondani Mulungu." Ici cioneka kuti ncostatheka kucitika, koma Buku Lopatulika litipatsa ife yankho. Ndi pakusunga lamulo laciwiri pamene timasunga loyamba. Pakuti Buku Lopatulika linena kuti. "Munthu akati, kuti, ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wace, ali wabodza; pakuti iye wosakonda mbale wace amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona. Ndipo lamulo ili tiri nalo locokera kwa Iye. Kutu iye amene akonda Mulungu akondenso mbale wace." (1 Yohane 4:20-21).

GAWO LACIWIRI: Kukonda awo amene ali m'mabanja antu.

Mulungu afuna kuti tidzikonda ao amene ali m'mabanja athu. "Akazi inu, mverani amuna anu, monga kuyenera mwa Ambuye. Amuna inu kondani akazi anu, ndipo musawawire mtima iwo. Ana inu, mverani akubala inu m'zonse, pakuti ici Ambuye akondwera naco. Atate inu, musaputa ana anu, kuti angataye mtima." (Akolose 3:18-21). Iyi ndiyo njira yomwe Mulungu anafunira kuti mabanja athu adzikhalira. Mkazi adzikonda mwamuna wace ndi kumacita zinthu izo zimene zingamkondweretse iye mu njira imodzi modzi yomwe akondera Mulungu ndi kumayesa kucita cinthu zimene zingamkondweretse. Mwamuna adzikonda mkazi wace ndi iye mwini. Yesu anati, "Cifukwa ca ici mwamuna adzasiya atate wace ndi amai wace nadziphatika yekha kwa mkazi wace, ndipo awiriwa adzakhalala m'modzi. Ndipo kotero salinso awiri

zitanthauza munthu wina aliyense. Ngati timkonda wina, sitidzacita kanthu kakuti kampweteke. Ngati matupi athu afuna kuti akhale olandirika kwa Mzimu Woyera sitingawacitse nchito za ucimo kutsutsana ndi Mulungu kapena munthu wina aliyense. Tidzicita zinthu zabwino zokha zokha.

GAWO LACITATU: Sungani kacisi kukhala wa ngwiro.

Mzimu Woyera safuna kukhala mthupi mwathu ngati maganizo athu sali otseguka kwa iye. Iye afunaso kuti akhale m'maganiziro athu. Ngati mafanisiro athu sali okondweretsa kwa iye, adzabwerera. Sadzafuna kukhala mwa ife. "Pakuti iwo amene ali monga mwa mzimu, asalalira zinthu za mzimu." (Aroma 5:8). Nthawi zina timaganiza za maganizo oipa ndikuganiza kuti palibe wina yemwe angadziwe. Komatu Mulungu amadziwa ganizo lathu liri lonse tiri nalo. Buku Lopatulika litiuza za zinthu zomwe tifuna kuti tidziganizira. "Cotsalira abale, zinthu ziri zonse zoonza, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, zoro zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli co koma mtima cina, kapena citamando cina, zilingirireni zii." (Afilipi 4:8).

Yesu anati m'Mateyu 5 ndi 6, kuti tisamaganiza za zinthu zomwe ziri zoipa kudzicita. Akuti nkucimwa ngakhake kuganiza za kucita cigololo kapena kupha, ngakhale kulekana ukwati kapena kunena bodza kapena kubwezera kapena udani wina ndi mnzace. Ngakhale pakupembedza Mulungu tiyenera kukhala osamalira kufuna ulemmerero kuti udzikhalala wa Mulungu osati ulemmerero wa ife eni. Tisamafuna kuti ena adziona kuti ifeyo ndiye timapembedza. Tidziyesa kucita

kuti maganizo athu adzikhala olandirika kwa Mzimu Woyera pomaganizira za zinthu zomwe angadzifune. Nthawi zina ici nco-bvuta kucicita. Mzimu Woyera amadziwa izi ndipo coteru adzatithandiza. Iye amadziwa zosowa zathu ngakhale ife eni sitidziona-tsa konse. Onani Aroma 8:26.

MTSOGOLERI:

Kacisi wa Mzimu Woyera si cinyumba cacikuru. Kacisi wa Mzimu Woyera ndi Mkristu amene amacita zomwe Mulungu afuna kuti acite. Iye amayesetsa kuti akhale monga momwe Mulungu afunira kuti akhalire. Kacisi wotereyu adzacititsa ena kuti adze kudzapembedza Mulungu. Adzakhala ngati "mudzi wokhazikika pamwamba paphiri." Ena adzaza kufunafuna Mzimu Woyera yemwe akhala mkacisi wotereyi.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

PHUNZIRO 10

MZIMU WOYERA, MZIMU WACIKONDI

VESI LOLOWEZA: *"Koma kunena za cikondano ca pa abale sikufunika kuti akulemberezi; pakuti wakukuphunzitsani ndi Mulungu kuti mukondane wina ndi mnzace."*

1 Atesalonika 4:9.

LEMBA LOWERENGA: Afilipi 2:1-2.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Yesu anapereka malamulo awiri akuru. Loyamba ndilo la kukonda Mulungu. Laciwiri ndilo lakukonda munthu. Koma ife tidziwa kuti popanda thandizo la Mulungu sitingathe kusunga limodzi la malamulowa konse. Tisanalole kuti Mzimu Woyera alowe m'mitima mwathu, tinali ndi nsanje ndi udani, kuposa mtima, mkangano, ndi maganizo oipa m'mitima mwathu. Nthawi zambiri zinthu zimenezi zinali kulamulira zocita zathu. Pamene Mzimu Woyera anadza m'mitima mwathu anatithandiza kuti tidzitsamalila tokha. Ucimo sunalinso mbuye wathu. "Cikondi ca Mulungu cinakhutulikwa m'mitima mwathu kupyolera mwa Mzimu Woyera amene anapatsidwa kwa ife." Ndipo conseco, Mulungu watipatsa ife nzeru zakutha kusunga malamulo ace.

GAWO LOYAMBA: Kukonda Mulungu.

Kodi tingaonetsere bwanji cikondi cathukwa Mulungu? Buku Lopatulika likuti,

37

palibe lamulo." Agalatiya 5:22-23. Izi ndizo zabwino zomwe sitingazigwiritse nchito mwa tokha. Pena nthawi zina tingakhale nazo zina za izo. Padzakhala nthawi pamene tiri kukonda. Nthawi zina tingakhale ndi cimwemwe kwa kanthawi kakafupi. Panthawi zina ndi zina tingakhale acifatso. Kapena tingakhale okoma mtima kwa kanthawi. Koma Mzimu Woyera yekha ndiye angathandize zonsezi kukula ndi kukhala ndi mizu m'moyo yathu.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amatithandiza kukhala ife eni.

Mzimu Woyera amapatsa mphatso kapena matelente kwa otsatira ace. Amatithandiza kukwaniritsa colinga cace ca moyo wathu. Werengani 1 Akorinto 12:4-11. Tidzikumbukira kuti zonse zomwe tingacite zimackera kwa Mulungu. Mphatso zathu tizidzigwiritse nchito monga momwe Mzimu Woyera atitsogolera. Tisamafunsa funso la matelente anthu kuti ali osiyana ndi a ena. Mulungu afuna kuti ena acite kanthu kena ndi anthu ena acite kanthu kena. Wina ali yense wa ife adzikhala woyamika kwa Mulungu kuti Mulungu anatipatsa ife talente lathulathu. Tizizindikira kuti Mzimu Woyera adzationetsa momwe tingacitire ndi nzeru zathuzo. Pomwepo tidzakhulupirira Mzimu Woyera kutitsogolera ndi myoyo yathu idzabwetetsa cimwemwe kwa Mulungu.

MTSOGOLERI:

Agalatiya 5:25 akuti, "Ngati tiri ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende." Ngati Mzimu Woyera watipatsa ife moyo tiyenera kuti zocita zathu zonse zicitike monga atitsogolera. Pomtsatira iye, tipeza cilungamo ndi mtendere ndi cimwemwe.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

PHUNZIRO 5

MZIMU WOYERA MU MPINGO

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera kumwamba."*
Luka 24:49.

LEMBA LOWERENGA: Macitidwe 2:38-47.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Mlungu wathu tinaphunzira za Mzimu Woyera mwa Mkristu ali yense payekha. Lero tidzaganizira za zomwe zingaoneke pamene Mzimu Woyera atha kulowa m'gulu la anthu, mpingo. Buku Lopatulika likuti mpingo ndi la Kristu. Thupi limeneli silingathe kukhala ndi moyo kufikira litadzazidwa ndi Mzimu wa Kristu. Mzimu ndiye amapatsa moyo. Mzimu Woyera ndiye amatsogolera mpingo. Popanda Mzimu Woyera, mpingo uli wakufa.

GAWO LOYAMBA: Mpingo udzipemphera kuti ukhale ndi Mphamvu.

Werengani Macitidwe 1:12-14. Mpingo woyamba kulandira Mzimu Woyera unali gulu la otsatira a Kristu mu Yerusalemu. Yesu anawauza iwo kuti akhalabe mu Yerusalemu ndi kuyembekeza kudza kwace kwa Mzimu Woyera. Iye anawalonjeza kuti Mzimu Woyera adzawapatsa iwo mphamvu. Ndipo iwo anamvera nakhalabe mu Yerusalemu. Iwo sanayesa

odwala kapena kutumikira osauka. Iwo anangokhala onse pamodzi mcipinda ca pamwamba kupemphera. Nchito ina iri yonse yomwe anaicita imene inalembedwa ndiyo yakusankha Mariya yemwe analowa m'malo a Yudas Iskariote kukhala mmodzi wa khumi ndi awiriro. Mpingo wopanda Mzimu Woyera unalibe mphamvu kufikira kwa ena. Koma pamene anali kupemphera iwaoanali kuyang'anira kudza kwa Mzimu Woyera.

Ngati mpingo wathu ulibe mphamvu zakulankhula ndi ena, tiyenera kupemphera kuti Mzimu Woyera adzaze mwa ziwalo zathu zampingo. Safuna kuti tidziyesa kucita nchito yace popanda Iye.

GAWO LACIWIRI: Mpingo uyenera kuonetsera Mphamvu imeneyi.

Pamene Mzimu Woyera anadza, anadzaza nyumba yonse momwe anali kukhalamo. Iye anadza pa wina aliyense. Ndipo onsewo amayemba kulankhula malilime acilendo omwe sanatha kulankhula kale konse. Mzimu Woyera anawapatsa uthenga ndi mau akuti alalikire. Ndipo iwo anayamba kupita m'miseu nayamba kuuza uthengawo kwa munthu aliyense amene anakomana naye. Mzinda unali wadzala ndi cipiringu ca anthu ocokera ku maiko ena amene anadza kudzakondwera phando la Pentekoste. Ndipo gulu linayamba kuwazungulira. Ndipo aliyense wapagulu lija anamva anthu aja ali kulankhula mu lilime lomwe iye anamva. Ndipo iwo sanamvesetsa kuti izi zinatha kucitika bwanji. Iwo anaona kuti ena a amene anali kulankhula aja sanali ophunzira bwino konse ai. Ndipo gulu la anthulo linali ndi cidwi cofuna kuti limve zambiri.

cifukwa cakuti iwo adzicitira mantha. Patso golo pace Paulo analemba, "Pakuti Mulungu sanatipatsa mzimu wa mantha; komatu wa mphamvu ndi cikondi ndi cidziletsa." (2 Timoteo 1:7). Tokha sitingathe kuima pa coonadi. Pamene anthu osakhulupira ati-funsa ife ndi kuyesa kutisokoneza ife, tiyenera kutsamira pa Mzimu Woyera kuti ati-thandize. 2 Timoteo 1:14 akuti, "Cosungitsa cokomaco udikire uwa Mzimu Woyera amenekhalitsa mwa ife."

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera amatithandiza kusamalira zilakolako zathu.

Sikuti koma tikhale m'mabvuto ndiye kuti titsamire pa Mzimu Woyera. Tsiku liri lonse zilakolako zathu zimatitsogolera kucoka kwa Mzimu. Pamene tiri kutsatira zilakolako zathu tidzisamalira kuti tisa-swa lamulo. Werengani Agalatiya 5:16-18. Ngati tatsogoleredwa ndi Mzimu Woyera sitidzaopa lamulo. Mzimu Woyera sadzatitsogolera kuti tikaswe lamulo. Ngati timtsatira, tidzacita koposa momwe lamulo lifunira.

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera amatithandiza kukhala ofanana ndi Mulungu.

Mzimu Woyera ndiye Nkhozwe wathu. Iye amatitsogolera kukhala munthu wabwino. Ngati Mzimu Woyera akhala mwa ife ndipo timulola kuti acite cifuniro cace, adzapindula "zipatso za mzimu". Cipatso cimenezi mwamsanga cidzakhala m'miyoyo yathu. Buku Lopatulika likuti, "Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso, pokana zimenezi

MZIMU WOYERA, NKHOSWE

VESI LOLOWEZA: *"Pakuti ufumu wa Mulungu sukhalakakudya ndi kumwa, koma cilungamo, ndi mten-dere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera."*

Aroma 14:17.

LEMBA LOWERENGA: Yohane 14:16-17.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Nthawi zambiri sitimadziwa kuti kodi tingacitenji kapena tinganenenji. Palibe cisankho cina ciri conse. Ngati pali nthawi, timapempha cilangizo kwa abwezi athu. Pena tingakhulupirire zomwe anena ndipo ndikucita zomwe alangizazo. Kapena nthawi zina timaganiza kuti cilangizo cace siciri cabwino ndipo siticitsatira conse. Mulungu anatipatsa ife Mzimu wace Woyera kutithandiza mu nthawi monga zimenezi. Nthawi zonse tingakhulupire zomwe wanena. Iye sadzalephera kutipatsa cilangizo cabwino.

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera amatithandiza kupeza yankho.

Werengani Luka 21:13-15. Yesu anadziwa kuti ophunzira oyamba adzaikidwa m'nden-de ndi cifukwa cotsatira iye. Iye anadziwa kuti adzafunsidwa mafunso ndi mafumu ndi olamulira. Koma Iye anawauza kuti asadera nkawa. Mu nthawi yotere, Mzimu Woyera adzawapatsa iwo mayankho. Panalibe

GAWO LACITATU: Mpingo uyenera kumafotokozaza Mphamvu zimenezi.

Ena a anthu anayamba kufunsa, "Kodi citanthauza ciani zimenezi?" Ndipo ena anati, "Aledzera." Koma Petro anamva mau amenewa ndipo anayamba kulalikira kwa gulu lija. Iye anawafotokozera momwe anthu amene anali kucita za cilendo aja sanali oledzera. Iye anawafotokozera momwe anadzazidwira ndi Mzimu Woyera. Ndipo anawafunsa kuti akumbukire uneneri wa Yoweli wakuti Mzimu wa Mulungu usadza ndipo anthu adzacita zinthu zodabwitsa. Werengani Yoweli 2:28-29. Iye anawafotokozera momwe kuuka kwa Yesu kunakwaniritsa uneneri wa Davide. Iye anawauzitsa kuti Yesu anawatumizira Mzimu Woyera. Ndi cifukwa cace zinthu zacilendozi zinali kuoneka.

Pamene Mzimu Woyera adzaza mpingo ziwalo zace sidzizacita manyazi kuuza ena. Iwo adzatsimikiza kuti Mzimu Woyera ali kuwatsogolera iwo. Ndipo iwo sadzakakapakucita zonse zimene Mzimu anena.

Awo amene anamvetsera Petro ali kulankhula anafunsa kuti kodi acite ciani. Ndipo Petro anawauza iwo kuti alape. Werengani Macitidwe 2:38-39. Tsiku limenelo anthu zikwi zitatu (3000) anapulumsidwa. Cifukwa Mzimu Woyera anawapatsa mphamvu, ophunzira owerengeka anadziwitsa ena, ena ambiri kulandira Yesu monga Ambuye. Pamene Mzimu Woyera adzaza gulu la Akristu, mpingo, amacita zinthu zazikuru zodabwitsa za Mulungu.

GAWO LACINAI: Mpingo uyenera kumagawana mphamvu imeneyi.

Onse ao amene analandira Mzimu Woyera pa tsiku la Pentekoste anali ayuda. Ndipo

pomwepo Ayudya onse anakhulupirira kuti Mzimu Woyera anali wa Ayuda okha. Koma nthawi ina patsogolo pace Mzimu Woyera analankhula kwa Petro. Anamuza kuti apite ndi anthu ena omwe sanali Ayuda. Pamene anamva mau a Mulungu, analapa. Ndipo pamene analapa, Mzimu Woyera anadza pa iwo monga momwe anacita pa Ayuda. Ndipo cinthu ici cinampangitsa Petro kudziwa kuti Mulungu afuna anthu amitundu yonse kumudziwa iye. Werengani Macitidwe 10:19-20, 44-47.

Mpingo womwe wadzala ndi Mzimu wa Mulungu sungasunge Mzimuwo kwa iwo okha konse ai. Iwo ali kukakamizidwa kuyesa kugawana ndi ena mphatso imenei kwa anthu onse amene awaona.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tipemphere kuti Mzimu Woyera adzaze mpingo wathu. Tiyeni timfunse kuti atithandize kuuza anthu ena onse za Yesu. Tilonjeze kutsegula mpingo wathu kwa ao onse amene anawapanga.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

Mzimu Woyera kuti adzatithandiza mu cisoni cathu. Iye adzatipatsa ife ciyembekezo. Pamene tiona anthu awiri ali kukwatirana, timakumbutsidwa ndi Mzimu Woyera kuti Mulungu amafuna kuti anthu adzikwatirana. Mulungu ali nayo nzeru ya banja kuti liphunzira za iye pamodzi. Ndi cifuniro ca Mulungu kuti mwamuna ndi mkazi amakhala munthu mmodzi ndikuti iwonse amakhala ndi ana. Iye afuna kuti tiwaphunzitse anawa za cikondi cace. Mu zinthu zonze zimene ticita, tidziyang'anyag'ana zomwe Mzimu Woyera ali kuyesa kutiphunzitsa.

MTSOGOLERI:

Mzimu Woyera anatumidwa ndi Mulungu kudzakhala mphunzitsi wathu. Iye afuna kutiphunzitsa kutanthauza kwace kwa moyo. Tingaphunzire kumvetsera ziphunzitso zace. Tiyeni tiyambe lero kufunafuna ciphunzitso ca Mzimu Woyera.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

Pamene tiri kuimba, angatitsogolere kumvetsa zomwe tiri kuimba, kotero kuti tikhoza kuimba mayamiko oonadi kwa Mulungu. Pamene tiri kupereka zopereka ndi zakhumi zathu, Mzimu Woyera angatithandize kukumbukira kuti Mulungu amatipatsa zonse zimene tiri nazo. Angatithandize kukumbukira kuti Mulungu amatipatsa zonse zimene tiri nazo. Angatithandize kuti tikhale opatsa okondwerera. Pamene timva mau a Mulungu kucoka kwa mlaliki, Mzimu Woyera angatipatsa ife kumvesetsa kwace. Ndipo pamene ali kuitana potsiriza pace pa msonkhano. Mzimu Woyera adzatiuza kuti kalipo kanthu kena komwe tingamcitire.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amatiphunzitsa m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.

Mzimu Woyera amatiphunzitsa tsiku ndi tsiku. Amatipangitsa kudziwa kuti Mulungu ndiye anapanga zokongola zimene tidziona. Mlengalenga, nyenyezi, mitengo, maluwa, mitsinje zonsezi ndi zace. Pamene tidziona Mzimu Woyera amatithandiza kukumbukira kuti Mulungu anapanga zonsezi kuti tikon-dwere nazo. Iye anapanga zinthu zabwino kuti tidzimve. Tingamwetulire pamene timva balame ziri kuimba liu lokoma mtima lone-nedwa ndi bwenzi. Tingayamike Mulungu cifukwa ca makutu omwe tiri nao kuti tidzimva. Mzimu Woyera amatikumbutsa kuti caku-dya cathu cimacokera kwa Mulungu. Amati-thandiza kuti tidzikhala oyamika pamene tiri kudya.

Pamene wina ali kudwala, Mzimu Woyera amatithandiza kudziwa kuti Mulungu safuna kuti wina wace adzibvutika. Mulungunso, amafuna kuti ao amene ali kudwala akhale bwino. Pamene pali imfa, tidzikhulupirira

PHUNZIRO 6

MZIMU WOYERA NDI A NCHITO ACE

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo ndinamva mau a Am-buye akuti, ndidzatumiza yani ndipo ndani adzatitumikira ife? Ndipo ine ndin-nati, ndine pano; munditumizeni ine."*

Yesaya 6:8.

LEMBA LOWERNEGA: Macitidwe 13:2.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Mkristu aliyense akhoza kutsogolere-dwa m'moyo wace wa tsiku ndi tsiku ndi Mzi-mu Woyera. Koma nthawi zina Mulungu amafuna munthu kuti acite nchito ina yapadera. Angafune munthu wina kuti akhale mtsogole-ri wotsogolera ena. Pena angafune munthu wina kuti adzipatule yekha kwa abwenzi ace ndi kupita ku malo ena kukauza ena za Yesu. Mkristu amene amatsatira Mzimu Woyera tsi-ku ndi tsiku adzaziwa ngati Mulungu ali kumitana kuti acite nchito ina.

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera amasankha atso-goleri a mpingo.

Mzimu Woyera adzikhala amene asankha ancito ace. Munthu sangadzisankhire yekha kugwirira nchito Mulungu. Ngati sanasankhidwa ndi Mzimu Woyera sadzakhala wokondwa mu nchito yace. Sadzadziwa njira yabwino koposa yakucitira nchito yace. Aliyense wa ife adzikhala wolola kucita nchito

mu mpingo. Koma tidzitsamira pa Mzimu Woyera kutitsogolera mu nchito imeneyi. Mzimu Woyera amalankhula kwa mpingo. Amawathandiza kudziwa awo amene wawasankha kuti agwire nchito ya utsogoleri. Onani Macitidwe 13:2.

Yesu amasamalira za mpingo. Iye afuna kuti atsogoleri ace adzikhala osamalira mu nchito zao. Iye afuna mpingo wace umtsatire. Ndipo coteri wa nchito wace ndi wakusonyesa anthu ena njira yakuti atsatire. Atsogoleri a mpingo adzikhala atumiki a mpingo. Koma iwo akhoza kutumukira mpingo pokhapo pamene ali kutumikira Ambuye. Macitifwe 20:28 akuti, "Tadzicenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira, kuti muwete Eklesia wa Mulungu umene anaugulu ndi mwazi wa Iye yekha."

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera amasankha amishonare.

Mulungu amafuna anthu ena kuti asiye abwenzi ao ndi mabanja awo ndi kupita ku malo ena. Iye ali kudziwa kuti anthu ambiri sali kumdziwa iye. Anthu ambiri sanamve za Yesu. Ndipo afuna wina kuti apite ndi kukauza anthu amenewa njira ya cipulumutso. Mzimu Woyera anatsogolera Paulo ndi Baranaba kumalo onga amenewa. Iwo ndiwo anali amishonare oyambira. Iye anawathandiza kudziwa komwe iye anafuna kuti apiteko. Iye anadziwa kuti m'mizinda ina anthu sanali okonzeka kulandira uthenga wace. Ndipo coteri sanalola Paulo ndi Baranaba kuti apite kumalo oterewo ai. Werengani Macitidwe 16:6-7. Mzimu Woyera anafuna kuti apite komwe angakagwiritse nchito nthawi mwanzeru. Ngati anakatalikira komwe Mzimu anawadziwitsa anthu anthu

atifotokozere zomwe tiwerenga. Pamene tiri kuwerenga, akhoza kutithandiza kumvetsetsa tanthauza lace. Iye angatitsogolere ife kuona momwe Lembalo lingacitire m'moyo wathu. Angatitsogolere kumvetsetsa zomwe Malemba atilangizira ife zomwe tingacite. Mzimu Woyera ndiye amamasulira mau amene tiwerenga m'Buku Lopatulika. Yesu anati, "Wopatsa moyo ndi mzimu; thupi silitandiza konse. Mau amene ndalankhula ndi inu ndiwo mzimu, ndi moyo." (Yohane 6:63). Ici ndico cifukwa cace mau a Yesu omwe analembedwa m'Buku Lopatulika ali ofunika kwambiri kwa ife. Mzimu Woyera amawapanigitsa kuti akhale mwa ife.

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera Amatiphunzitsa pamene tiri kupemphera.

Kupemphera ndiko kulankhula ndi Mulungu ndi kumvetsera kwa Mulungu. Pamene Mulungu ali kulankhula, amalankhula nafe kupyolera mwa Mzimu Woyera. Mzimu Woyera amaticititsa kuti tidziwe zinthu zomwe tingapempherere. Buku Lopatulika likuti tiri nazo zosowa zakuya koposa koteri kuti sitingathe kudzinena m'mau. Mzimu Woyera amatifotokozera zosowa zimenezi. Mzimu Woyera amatithandiza kumvetsetsa za ukuru wace wa Mulungu koteri kuti mitima yathu imadzala ndi mayamiko. Ndipo tingaphunzire kucokera kwa Mzimu Woyera kukonda ena koteri kuti timadandaulira moona mtima kwa Mulungu kuti awathandize.

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera amatiphunzitsa ku calici.

Mzimu Woyera amatiphunzitsa pamene tipita ku calici. Pamene tiri kuphunzira phunziro lathu la Sande Skulu, angatiphunzitsa momwe tingakhalire mwakufuna kwace.

MZIMU WOYERA, MPHUNZITSA

VESI LOLOWEZA: *"Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyu adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu."*

Yohane 14:26.

LEMBA LOWERENGA: Yohane 6:45.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Mphunzitsi amatilangiza ife nzeru zomwe tingakhaliro naco moyo wabwino. Pena tingamve mphunzitsi ali kufotokoza momwe tingacitire kanthu kena. Pena ife tinganene kuti, "Indedi, ndi nzeru yabwino imeneyi." Koma mpaka titayesa kucita ife tokha, sitidziwadi kuti iyi ndi nzeru ya bwino. Buku Lopatulika linena kuti Mzimu Woyera adzatiphunzitsa ife. Ngati tiphunzira maphunziro athu bwino lomwe, pomwepo tidzakhala molingana ndi ziphunzitso zimenezi. Tidzawagwiritsa nchito maphunziro amenewa m'mabanja anthu, pa nchito, mu calici (mumpingo) pa msiku, kapena kwina kuli konse komwe tipita.

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera amatiphunzitsa kupyolera M'Buku Lopatulika.

Nthawi iri yonse pamene tiwerenga Buku Lopatulika, tidzifunsa Mzimu Woyera kuti

akadadza kwa Yesu. Ngati timlola iye, adzatitsogolera mu njira yonga imeneyi lero lino. Iye adzatithandiza kumuka komwa zincito zathu zidzadzetsa ulemmerero kwa Mulungu.

GAWO LACITATU:

Nthawi zina timacita mantha ndi man-yazi kunena za Yesu. Mzimu Woyera adzatilimbitsa ife. Mzimu Woyera anapatsa aneneri mphamvu ndi kulimba mtima. Ndipo iwo anadzudzula mtundu wonse za ucimo. Iwo ananena momwe Mulungu adzalangira Israeli cifukwa ca ucimo. Werengani Mika 3:8. Mzimu Woyera anapatsa Yohane Mbatizi kulimba mtima kudzudzula Herode za cigololo. Petro analandira kulimba mtima kulan-khula ndi olamulira za uthenga wa Yesu. Olamulira amenewa anali nayo mphamvu yakumuika Petro mu ndende cifukwa cakulankhula mau amenewa. Koma Mzimu Woyera anamthandiza kuwalalikira iwo. Akristu ena oyamba analandira kulimba mtima kucoka mwa Mzimu Woyera. Ndipo iwo anauza uthenga wace kwa ambiri. Macitidwe 4:31 akuti, "Ndipo m'mene adapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene adasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mau a Mulungu molimbika mtima." Mzimu Woyera samatsogolera anthu ace ancito kucita nchito osawapatsanazo mphamvu yakucita ncito.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amasankha ena kupemphera.

Mulungu samasankha atsogoleri ndi kusiyana kuti angokhala otsatira. Iye a ali ndi nzeru ya kwa ao amene atsatira. Iye afuna kuti Mkristu aliyense adzipempherera ao amene atsogolera. Iye afuna

kuti tidziwe kusowa kwace kwa ao amene
atsogolera; pena lai ndi zosowa za thupi.
Angalankhula nafe ndi kutifunsa kuti ti-
thandize popeza zosowazo. Mzimu Woyera
afuna Akristu adzipemphererani wina ndi
mzace. Ife afuna ife tonse kumtsatira
pamodzi. Aefesi 6:17-18, "Mutengenso ci-
soti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu
ndilo Mau a Mulungu, mwa pemphero londe
ndi pembedzo mupemphere nthawi yonse mwa
Mzimu, ndipo pocazera pamenepo cicezerere
ndi kupembedzera oyera mtima onse."

MTSOGOLERI:

Pa nchito zina Mulungu amaitana mun-
thu mmodzi. Mzimu Woyera amalankhula kwa
munthu ameneyo. Iye adzikhala wolola kum-
vera. Ena Mulungu sawaitanira nchito yo-
tereyi. Koma Mulungu ayembekezera kuti
iwo adzimtsatira iye ndi kumapempherera
ancito amene anawaitana.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

Mulungu adzamuthandiza kudziwa zabwino ndi
zoipa. Tiyezi tipemphere kuti anthu ambiri
adzakhulupirira Mzimu Woyera ndi kumvetse-
ra pamene ali kulankhula m'mitima yao.

Mwana wa Mulungu amene acita ucimo
nayenso ayenera kucita cisankho. Ngati
asankha kukana kutsatira Mzimu Woyera,
iye adzapitirirabe kukhala munthu wosakon-
dwa. Iye adzafunafuna mtendere mu mtima
mwace komwe osaupeza. Koma akasankha ku-
lapa macimo ace ndi kutsatira Mzimu Woyera,
ndipono Mzimu adzam'thandiza iye kuyamban-
so kukula monga Mkristu.

Tiyezi tipempherere Akristu anzathu
omwe alephera kukhala otsatira oona a Yesu.
Tiyezi tipemphere kuti amve liu la Mzimu
Woyera ndi kufunafuna cikhululukiro cace,
koterokuti adzawapatsa iwo mtendere.

NYIMBO YA AZIMAI:

PEMPHERO:

ooOoo

Ngati amkhulupiriradi ndi kukhulupirira Yesu, pomwepo Yesu amawapatsa Mzimu Woyera kuti akhale mwa iwo nthawi zonse. Iwo akhululukidwa macimo ao ndipo ayamba kuphunzira kukhala moyo waukuru wocuruka.

GAWO LACINAI: Mzimu Woyera amalowa mwa cikhulupiro.

Sitingakwanire kuti tikakamize Mzimu Woyera adze ndi kukhala mwa ife. Pali njira imodzi yokha yakulandirira Mzimu Woyera. Ndiyo yakukhala naco cikhulupiro mwa Mzimu Woyera ndi kukhulupiro. Sitingakhulupirire zincito zabwino zokha kukhala zokwanira. Tidzikhululupirirabe kuti Mzimu Woyera amatitsogolera ife mu njira zoyenera. Iye yekha ndiye angatithandize kukhala moyo wa Cikristu. Werengani Agalatiya 3:2-3. Anthu aku Agalatiya analeka kutsatira Mzimu Woyera tsiku ndi tsiku. Paulo anawakumbutsa kuti ao amene analandira Mzimu Woyera ayenera kupitilira kumtsatira. Ndipo pomwepo Mzimu Woyera, yemwe Yesu anapereka, amakhala ngati kasupe wa madzi yemwe amazdetsa cimwemwe ndi mtendere. Werengani Yohane 4:14.

MTSOGOLERI:

Munthu wocimwa wotaika ayenera kusanakha. Iye akhoza kukana thandizo la Mzimu Woyera; ndipo pomwepo Mzimu Woyera sakhoza kumthandiza. Ndipo iye adzakhalabe kapolo wa ucimo. Kapena wocimwa uja angamvere pamene Mzimu Woyera ali kulankhula. Iye akhoza kukhulupirira Mzimu Woyera ndi kulandira cipulumutso kucoka ku macimo comwe Yesu acipereka. Ndipo iye akhoza kutitirizabe moyo wace wonse kutsatira Mzimu Woyera. Mzimu Woyera adzathandiza iye kumvesetsa ziphunzitso za Yesu. Mzimu wa

PHUNZIRO 7

MZIMU WOYERA NDI MUNTHU WOCIMWA

VESI LOLOWEZA: *"Tsoka kwa ana opanduka, ati Yehova, amene atenga upungu koma si pa Ine; napanga mapangano opanda mzimu wanga, kuti aonjezere cimo ndi cimo."*

Yesaya 30:1.

LEMBA LOWERENGA: Tito 3:5-6.

ZOPEMPHERERA:

PEMPHERO:

MTSOGOLERI:

Monga takhala tiri kuphunzira za Mzimu Woyera, tanena kuti Mzimu Woyera amathandiza ao amene amtsatira Iye. Nanga bwanji ao amene akana kumtsatira? Buku Lopatulika limawachula anthu oterewa kuti anthu ocimwa. Aliyense wa ife ndi munthu wocimwa. Ngakhale tinakhululukidwa ndi Yesu, timacimwabe. Nthawi iri yomwe tisankha ku kuti ticite kanthu kena komwe Mzimu Woyera safuna kuti tika, tiri kucita ucimo. Nthawi iri yonse pamene tikana kucita zomwe Mzimu Woyera atitsogolera kuti ticite, tiri kucita ucimo. Kodi Mzimu Woyera amalankhula bwanji kwa anthu ocimwa?

GAWO LOYAMBA: Mzimu Woyera angalankhule kupyolera mwa ena.

Mulungu akonda anthu onse. Ndico cifukwa cace afuna kuwapulumutsa kocoka ku ucimo. Mzimu Woyera amalankhula kwa munthu

wotaika ndi kumudandaulira kuti akhulupirire mwa Yesu. Mulungu amalankhula ndi mwana wace amene acita ucimo kumukakamiza kuti adzikhala moyo wa Cikristu. Mzimu Woyera angalankhule mwa akapolo ace alaliki. Mlaliki anganene kanthu kena komwe kangampangitse munthu wocimwa kuganizira za macimo. Ndi wocimwa uja angamvere cisoni macimo ace. Kapena mlaliki anganene za cikhodi ca Mulungu ndipo wocimwa uja angafune kuti akhululukidwe kotero kuti adziwe zambiri za cikondi cimeneci. Pena Mzimu Woyera angagwiritse nchito munthu wina aliyense. Pena angagwiritse nchito bwenzi kuuza wocimwa uja za njira ya Mulungu. Nthawi zina Mzimu Woyera sangalankhule kupyolera mwa munthu wina konse ai. Angangolankhula kwa munthu mwini yekha. Nthawi zina timacula njira imeneyi "liu laling'ono lonong'ona." Ici citanthauza kuti timamva pansi mkati mwathu kuti tiyenera kucita kanthu kena. Pena tingamve wina ali kulankhula mkati mwathu. Liu limeneli lingamkakamize wocimwa uja kuti alape. Iye angadziwe kuti ayenera kukhulupirira Yesu kuti ampulumutse. Kapena ngati wapulumutsidwa kale, angadziwe kufunika kwace kwakuti atembenke kucoka ku macimo ace kuti akhale wotsatira woona ya Yesu. Mzimu Woyera angalankhule ndi anthu njira zambiri. Pamene munthu aganiza kuti pena Mzimu Woyera angamalankhule naye ayenera kumvetsera mosamalitsa. Buku Lopatulika linena kuti, "Musazime Mzimuyo." (1 Atesalonika 5:19). "Momwemo, monga anena Mzimu Woyera, 'Lero ngati mudzamva mau ace, Musaumitse mitima yanu, monga m'kupetsa mtimamo, monga muja tsiku la ciyesero m'cipululu.'" (Ahebri 3:7-8).

GAWO LACIWIRI: Mzimu Woyera angaleke kulankhula.

Mzimu Woyera sadza itana nthawi zonse. Sadzadandaulirabe anthu kuti amtsatire iye. Ngati munthu sadzamvera Mzimu wa Mulungu, Mzimu udzamsiya munthuyo. Mu Aroma Mutu 1 Buku Lopatulika litusa momwe anthu amuna ndi akazi anapitirirabe kucimwira Mulungu. Potsiriza pace Mulungu anawalekerela m'macimoao. Mulungu analola kuti atengeke ndi ucimo. Analola ucimo kuti ulamulire myoyo yao. Mu Miyambo 1:24-28 Mulungu anene kuti sadzathandiza ao amene anamkana iye. Pamene ucimo udzetsa kusakonkwa m'myoyo yao, sadzawathandiza. Pamene aitanira pa iye, sadzawayankha. Sadzampeza. Munthu ayenera kumamvera pamene Mzimu Woyera ali kulankhula kwa iye. Sitinganene kuti, "Tileke, pamene ndidzakonzeka, ndidzaitana Mzimu Woyera." Pena sitidzatha kumpeza pamene tidzaitana pa iye.

GAWO LACITATU: Mzimu Woyera afuna kuti adzimvedwa.

Anthu ena omwe amva Mzimu Woyera ali kulankhula kwa iwo kuti azindikire ucimo wao. Iwo afuna kuti akhululukidwe. Iwo afuna kumva kuti ali oyera mkati. Iwo kukhala afulu ku ucimo womwe anali kuucitabe. Iwo adziwa kuti sangadzimasule okha. Ndipo coteri amamvetsera kwa Mzimu Woyera. Anthu amenewa afuna kufziwa njira ya Mzimu Woyera. Iwo afuna kudziwa momwe Mzimu Woyera angawathandizire kuti apeze cipulumutso. Pamene amva mlaliki kapena kuwerenga m'Buku Lopatulika lao kapena kulandira cilangizo cocokera kwa abwenzi ao, iwo ali kumvera Mzimu Woyera. Iye amawathandiza kuti adziwe momwe angadziwire ngati zomwe ali kumva kapena kuwerenga ziri zoonadi.